AL-MAHMOOD

Your gateway to Islamic knowledge

BUKU LA MAINA ASILAMU

COURTESY OF :
AL MAHMOOD PUBLICATIONS

AL-MAHMOOD

Your gateway to Islamic knowledge

EDITION ONE: 2016

COURTESY
of
AL - MAHMOOD PUBLICATIONS
P.O. Box 739, Lilongwe, Malawi

CELL: +265 999 226 120 / 999 855 000 / 999 300 786
E-mail: asb.publications@ymail.com

HOTLINE:0995778788

FOREWORD

KUMUTCHA DZINA KWA MWANA

Ndi mphatso ya pamwamba kwa munthu msilamu kupatsidwa dzina labwino. Kotero kuti pofuna kusankha dzina la mwana, Kumakumbukiranso kuti dzinalo limatha kukhala ndi zotsatira zake zabwino kapena zoipa pa mwanayo.

UBWINO OSANKHA DZINA LABWINO

- Ibn Umar R.A anati; mtumiki wa Allah S.A.W anati: Mayina okondedwa kwambiri kwa Allah S.W ndi Abdullah komanso Abdul-Rahmaan" (muslim)
- Mtumiki S.A.W anati, "kwa munthu amene angapatsidwe dzina ngati langa, akufuna madalitso anga, iye adzadalitsidwa kum'mawa kulikonse komanso kumadzulo mpaka tsiku la Qiyamah"(kanzul – ummaal)
- Mtumiki S.A.W anati: "munthu amene wabadwa mwana wa mamuna namutcha kuti Muhammad, chifukwa chondikonda ine ndikufuna madalitso a dzina langa, adzakhala iye ndi mwana wake ku jannah" (kanzul – ummaal)
- Mtumiki S.A.W anati: "ndithu inu anthu tsiku la Qiyamah mudzakhala mukuyitanidwa ndi maina anu ndi maina a azibambo anu, choncho mudzipereka maina abwino". (Aboo Dawood)

Chinali chizolowezi cha mtumiki S.A.W kufufuza maina a anthu komanso midzi. Kotero kuti ngati dzina la munthuyo kapena mudziwo lili labwino, iye anali kusangalala, ndipo izi zimaonekera pankhope pake. Ngati limakhala loipa iye samasangalala.

Chifukwa cha chidwi chake pa maina abwino, iye anali kusintha maina oipa. Kotero kuti nthawi ina mtumiki S.A.W adafunsa ngati wina angazipereke kukama Ngamila nkaka. Munthu wina adazipereka. Mtumiki (S.A.W) adamufunsa dzina lake ndipo adati: "iwe dzina lako ndani?" iye adati, ndine 'HARB'. Mtumiki (S.A.W) anati kwa iye khala pansi, ndipo sadamulole kuti akame nkaka, chifukwa dzina lake anali 'HARB' (kutanthauza kuti Nkhondo) zomwe sizikupeleka chisangalatso.

Kotero kuti mtumiki (S.A.W) adafusanso kuti: Ndani akame mkaka? Munthu wina wachiwiri adaima nati ine. Mtumiki (S.A.W) adamufunsa dzina lake, iye adati ndine “YA'EESH”. (Kutanthauza kuti kukhala ndi moyo wautali). Mtumiki (S.A.W) anati kwa iye: kama mkaka wake. (AL-MUWATA'A).

Aishah (R.A) anati: “ndithu mtumiki (S.A.W) anali kusintha dzina loipa. TIRMIDHI

Tatiyeni asilamu timusankhire mwana wathu dzina labwino. Kugwiritsa ntchito maina a atumiki a Allah, maswahaba ndi a anthu ena omuopa Allah (S.W) komanso okondedwa ndi Allah (S.W), ndi njira imodzi yopezera madalitso.

1. NOTE: DZIWANI IZI:

Ngati mwana apatsidwa dzina lomwe ndi limodzi mwa maina a Allah (S.W), ndiye kuti ndikoyenera kuti kumayambiliro kwake tizi gwiritsa ntchito mau oti “ABDU” kutanthauza kuti kapolo. Monga “Abdullah”, kutanthauza kuti kapolo wa Allah.

2. NOTE: DZIWANI:

Ndibwino tikamamuyitana mwana wathu, tizinena dzina lonse monga “Abdullah” osamuyitana mwachidule kuti Abudu. Kapena kungoti Azizi mimalo moitana Abdul Aziz, kapenanso kungoti 'Muha' mimalo monena Muhammad. Komanso katchulidwe ka zilembo za dzinalo tiziyesetsa kuti kadzikhala kabwino. Tiziyesetsanso kudziwa tanthauzo la dzinalo ngati liri la chilankhulo chachilendo.

Tsopano tibweretsa ena mwa maina abwino kuti chikhale chitsanzo:

MAINA A ZIBAMBO

A

Aadam: آدم. **Ndi dzina la mneneri komanso ndi munthu oyamba kulengedwa ndikutumizidwa pa dziko la pansi.**
Aadil: عادل **wachilungamo. Swifat ya mtumiki (S.A.W)**
Aaqil: عاقل **wanzeru.**
Aatiq: عاتق **omasulidwa.**
Abdullah عبد الله **Kapolo wa Allah. limeneli linali dzina lokondedwa kwa mtumiki (S.A.W)**

B

Baraa: براء **omasuka, oyela. Dzina la swahabah (R.A).**
Basheer: بشير **obweretsa nkhani yabwino**
Bilaal: بلال **wopambana. Dzina la swahaabah odziwika bwino amene amachita adhaan nthawi ya mtumiki (S.A.W).**
Burhaan: برهان **umboni kapena kuti chigomezero.**
Bishr: بشر **chisangalalo-nkhani yabwino. Dzina la swahabah (R.A).**

D

Dawood: داود **dzina la mneneri odziwika wa Allah.**
Dhaakir: ذاكر **womukumbukira Allah kwambiri.**

E

E'Jaz: إعجاز **kuchita chinthu choti ena sangachikwanits**

F

Faarooq: فاروق **osiyanitsa pakati pa choonadi ndi bodza.**
Farhaan: فرحان **wosangalala kwambiri**

G

Ghazawaan: غزوان **dzina la swahabah.**

H

Haabeel: هابيل **dzina la mwana wa Adam (A.S).**
Haroon: هارون **dzina la mtumiki wa Allah.**
Haamid: حامد **wotamanda.**
Hassan: حسن **wabwino, dzina la chidzukulu cha mtumiki (S.A.W).**
Hussein: حسين **chidzukulu cha mtumiki (S.A.W).**

I

Ibrahim: إبراهيم **Dzina la mtumiki wa Allah.**
Idrees: إدريس **Dzina la mtumiki wa Allah.**
Ilyas: إلياس **Dzina la mtumiki wa Allah.**

J

Jafar: جعفر **Dzina la Swahabah (R.A).**
Jaabir: جابر **Dzina la Swahabah (R.A).**
Jamaal: جمال **Kukongola.**

K

Ka'b: كعب **dzina la swahabah (R.A).**
Kaamil: كامل **wokwanila.**
Khabbaab: خباب **dzina la swahabah (R.A).**

L

Loot: لوط **dzina la mneneri wa Allah.**
Luqmaan: لقمان **dzina la munthu odziwika bwino ku nzeru zakuya.**

M

Mas'ood: مسعود **wamwayi. Dzina la swahabah (R.A).**
Mahfoodh: محفوظ **otetezedwa.**
Miqdaad: مقداد **dzina la swahaabah (R.A).**
Muzzammil: مزمل **dzina lina la mtumiki (S.A.W)**

N

Nooh: نوح dzina la mtumiki wa Allah.
Nu'maan: نعمان dzina la swahabah (R.A).

Q

Qaasim: قاسم ogawa, dzina la mwana wa mtumiki (S.A.W).
Qais: قيس dzina la swahabah (R.A).

R

Rafeeq: رفيق bwenzi,
Raashid: راشد otsata njira yachilungamo.
Raafi: رافع wapamwamba, dzina la swahabah (R.A).

S

Sa'd: سعد mwayi, dzina la swahabah (R.A).
Saabir: صابر wopilira.
Shaafee: شافي wochiza, opepesera mzake.

T

Thaabit: ثابت dzina la swahabah (R.A).
Taha: طه dzina la surah mu Qur'an.
Taariq: طارق nyenyezi ya ku m'mawa.
Talhah: طلحة dzina la swahabah (R.A).
Tawfeeq: توفيق opatsidwa kuthekera ndi Allah.

U

Ubadah: عبادة kupembedza: dzina la swahabah (R.A).
Ubayy: أبي okana kuchita zoipa: dzina la swahabah (R.A).
Umar: عمر wa umoyo wautali: dzina la swahabah (R.A) yemwe adalinso khalifah wachiwiri.
Usamah: أسامة mkango. Dzina la swahabah (R.A).

W

Waabisah: وابصة **dzina la swahabah (R.A).**
Wahaab: وهب **mphatso: dzina la swahabah (R.A).**
Wakeel: وكيل **othandiza nzeru potheta mabvuto mwaubwino.**

Y

Ya'qoob: يعقوب **dzina la mneneri wa Allah.**
Yaaseen: ياسين **dzina la surah mu Qur'an.**
Yaasir: ياسر **zopepuka, dzina la swahabah (R.A).**
Yusuf: يوسف **dzina la mneneri wa Allah.**

Z.

Zhaakir: ذاكر **omukumbuka Allah kwambiri.**
Zaid: زيد **dzina la swahabah (R.A).**
Zubair: زبير **ochenjera ndi wa nzeru. Dzina la swahabah (R.A).**

MAINA A CHIKADZI

A

Aaishah: عائشة **Dzina la Mkadzi wa mtumiki Muhammad (S.A.W).**
Aleemah: عليمة **Mkazi wophunzira kwambiri.**
Amatullah: أمة الله **Mdzakazi wa Allah.**
Aqeelah: عقيلة **Mkadzi wa mzeru.**
Ameenah: آمنة **Wokhulupilika.**
Aasimah: عاصمة **Mkadzi owateteza anthu ena.**

B

Basheerah: بشيرة **Dzina la swahabah wa chi kadzi.**
Bareerah: بريرة **Dzina la Sahaabiya (R.A).**
Barakat: بركة **Madalitso.**

D

Dhaakirah: ذاكرة **Omukumbuka Allah kwambiri.**
Dhakiyyah: ذكية **Mkadzi wanzeru.**

F

Faadhilah: فاضلة **Phindu.**
Faaizah: فائزة **Kupambana.**
Feeroozah: فيروزة **Mwala wa mtengo wapatali.**
Fatimah فاطمة **Mwana wa mtumiki (S.A.W).**
Foziah: فوزية **Kupambana.**

G

Ghaaziyah: غازية **Mkadzi womenya nkhondo.**

H

Haajirah: هاجرة **Mkadzi wa hazrat Ibrahim.**
Haamidah: حامدة **Woyamika, Wotamanda.**
Haafizah: حافظة **Amene akudziwa Qur'an yonse pa mtima.**
Habeebah: حبيبة **Wokondedwa.**
Hafeedhah: حفيظة **Wotetezedwa.**
Hafsah: حفصة **Dzina la mkadzi Wamtumiki (S.A.W).**
Hakeemah: حكيمة **Waluntha.**
Hanifah: حنيفة **Okhulupirira wo wonadi.**
Hawwaa: حواء **Amene amakana za bodza ndi kutsatila choonadi. Mkadzi wa Hazrat Aadam**
Husnaa: حسنى **Womuopa Mulungu, Wokongola.**

I

Iffat: عفة **Wodzisunga. Izzat:** عزة **Ulemelero**

J

Jameelah: جميلة **Wokongola.**
Jaariyah: جارية **Mdzakazi.**
Juwairiyah: جويرية **Mkadzi Wamtumiki (S.A.W)**

K

Kareemah: كريمة **Dzina la Sahaabiyyah.**
Khadijah: خديجة **Hazrat Khadija anali Mkadzi woyamba wa Mtumiki (S.A.W).**
Khaarijah: خارجة **Dzina la Sahabi amene ana menya nawo nkhondo ya Badr.**
Kareemah: كريمة **Wolemekezeka.**
Khairah: خيرة **Wabwino.**
Kulthoom: كلثوم **Dzina la Sahaabiyah(R.A)**

L

Labeebah: لبيبة **Mkadzi wa nzeru: Dzina la Sahaabiyyah (R.A).**
Lailaa: ليلى **Dzina la Sahaabiyah (R.A).**
Lubaabah: لبابة **Wanzeru, Dzina la Sahaabiyah (R.A)**

M

Ma'soomah: معصومة **Otetezedwa**
Maahirah: ماهرة **Katswiri.**
Mahfoozah: محفوظة **Wotetezedwa.**
Mahmoodah: محمودة **Woyamikidwa.**
Maimoonah: ميمونة **Dzina la mayi wa okhuhipihira mkadzi wa Mtumiki(S.A.W).**
Mansoorah: منصورة **Wopulumutsidwa.**

N

Na'eemah: نعيمة **Mtendere.**
Naadirah: نادرة **Chisankho wosowa.**
Nabeelah: نبيلة **Okongola, wanzeru.**
Nadeemah: نديمة **Bwenzi, bwanawe.**
Najmah: نجمة **Nyenyezi.**
Naqeebah: نقيبة **Msogoleli, nthumwi.**

Q

Qamar: قمر **Mwadzi mwezi.**
Qareebah: قريبة **Pafupi, wapafupi, kuyandikira.**

R

Raeesah: رئيسة **Mtsogoleli, Mfumu.**
Raabitah: رابطة **Munthu amene akulumikiza pakhati pa zinthu ziwiri .**
Raafiah: رافعة **Wapamwamba,wachuma.**
Radhiyyah: رضية **Wosangalalidwa, woyanjidwa.**

S

Saa'irah: سائرة **Dzina la Sahaabiyah (R.A).**
Saabiqah: سابقة **Wotsogola.**
Sa'diyyah: سعدية **Odalitsidwa.**
Sa'eedah: سعيدة **Wamwayi.**
Saabirah: صابرة **Wopirira.**
Saajidah: ساجدة **Munthu wogwesa nkhope pansi kulambira mulungu.**
Saalihah: صالحة **Owopa mulungu (wabwino).**
Saarah: سارة **Wosangalala, mkadzi wa Hazrat Ibrahim (A.S).**

T

Taaibah: تائبة **Wolapa machismo zoipa.**
Taahirah: طاهرة **Woyera.**
Tayyibah: طيبة **Wabwino.**
Thamrah: ثمرة **Chipatso.**

U

Ummu Fakeeh: أم فكيه **Dzina la Sahaabiyah (R.A).**
Ummu Habibah: أم حبيبة **Dzina la mkazi wa Mtumiki (S.A.W).**
Ummu Haraam: أم حرام **Dzina la Sahaabiyah (R.A).**
Ummu Kulthoom: أم كلثوم **Dzina la mwana wa chikadzi wa Mtumiki (S.A.W).**
Ummu Sulaim: أم سليم **Dzina la Sahaabiya (R.A).**

W

Waahibah: واهبة **Mkadzi wopeleka.**
Waahidah: واحدة **Mmodzi.**
Wazeerah: وزيرة **Nduna ya chikazi.**

Y

Yaasmeen: ياسمين **Duwa la fungo lonunkhira.**
Yusairah: يسيرة **Kumanzele.**

Z

Zainab: زين ب **Dzina la mwana wa Mtumiki (S.A.W) komanso ndi zina la mkadzi wa Mtumiki (S.A.W).**
Zeenat: زين ت **Kukongola kukongoletsa.**
Zaitoonah: زيتونة **Mtengo wa olive.**
Zakiyyah: زكية **Wanzeru.**
Zameelah: زميلة **Bwenzi.**
Zarqaa: زرقا **Mthindi wa blue.**

ZOYENERA KUCHITA MWANA AKABADWA

Mwana akangobadwa asambitsidwe. Makolo apemphe a sheikh kapena msilamu aliyense wabwino, owopa Allah kuti achite adhaan kuti achite adhaan ku khutu la kumanja kwa mwanayo komanso Iqaamah ku khutu la kumanzere kwake.Ubwino wake ndiwakuti; uthenga wa chisilamu, ukulu ndi umodzi wa Allah (S.W), komanso uthenga wa mtumiki (S.A.W), ukafike pansi pa mtima wake, kuti in-sha-allah adzakule ali msilamu otsatira malamulo a Allah ndi mtumiki wake.
Kenako amuchitire dua monga (Allahuma inni uidhuha/ bika wa dhurriyyataha minash-shaitaanir –rajeem).

TANTHAUZO:
O: Allah, ndikupempha chitetezo chanu pa iye ndi ana ake kwa satana wothamangitsidwa.

TAH'NEEK:

Uku ndiko kuika kachidutswa kotafuna tafuna kale mkamwa mwa mwanayo. Nthawi zambiri kamakhala kachidutswa ka Tende. Ngati palibe Tende, uchi ukhoza kugwiritsidwa ntchito. Kuteloku ndi sunnah chifukwa mtumiki (S.A.W) adachita Tah'neek kwa maswahaba ake awiri, omwe ndi Abdullah ibn Zubair ndi Abdullah ibn Twalha (R.A).

KUMETA TSITSI, AQEEQAH NDI KUMUTCHA DZINA

Ndi sunnah pa tsiku la chisanu ndi chiwiri (7) chibadwireni cha mwanayo, kumeta tsitsi lake. Kuteloku pa shariah kumatchedwa kuti Aqeeqah (kumeta koyamba kwa m'mutu), komanso kuzinga chinyama. Mwana wa mamuna mbuzi ziwiri ndipo wa mkazi imodzi. Kenako timusankhire dzina labwino loyenera.

Tsitsi lamwana likametedwa, liyesedwe pa sikelo ndipo ndalama zofanana mulingo ndi tsitsilo zipelekedwe mwaulele (sadaqah)

kwa osowa, m'banja momwemo kapena wina aliyense. Kenako tsitsilo likwililidwe pansi. (pa malo abwino).

MDULIDWE

Kuchita mdulidwe ndi sunnah. Tidziyesetsa makamaka mwanayo asanakwanitse zaka zisanu ndi ziwiri (7). Pomwe tikufuna kumuchita mdulidwe mwana, tayenera kulingalira za umoyo ndi thanzi lake. Kotero kuti sikoyenera kumuchita mdulidwe pomwe iye akudwala, koma pomwe ali bwino.

DZIWANI IZI:

Ngati mzimayi oyembekezera akupita kuchipatala kuti akachile, atenge pamodzi ndi iye chili chonse choti ndi kugwiritsa ntchito posungila mchombo wamwanayo omwe umadulidwa, monga kontena. tikabwelera nawo kunyumba tidzaukwilire pansi. izi ziri chonchi chifukwa chakuti chisilamu chikutiphunzitsa kusamala chirichonse chokhudzana ndi thupi lathu monga ngati tsitsi, makadabo ndi zina zotero.

Choncho, ngati tingazisiye kuchipatala ndiye kuti ife sitidziwa kuti azisamala kapena ayi. Ndiye ndi udindo wathu kuwonetsetsa kuti mchombo umenewu ukusamalidwa.

ngati tingafune kudziwa zambiri za matanthauzo a maina kapena tikufuna kupereka dzina ndiye tikukaikira za tanthauzo lake, imbani foni ku manambala awa:

0995569750
0993977513
0993218907

NOTES

NOTES

NOTES

COURTESY
of
AL - MAHMOOD PUBLICATIONS
P.O. Box 739, Lilongwe, Malawi
CELL: +265 999 226 120
+265 999 855 000
+265 999 300 786
E-mail: asb.publications@ymail.com
HOTLINE:0995778788